



In-Depth Interviews with Household Members

Opening statements:

Zikomo povomereza kuyankha mafunso okhudza inuyo komanso maganizo anu pa nkhanu ya munthu kuziyeza yekha kuti adziwe ngati ali ndi kachilombo koyambitsa matenda a Edzi. Kucheza kwathu mwina kutitengera pafupifupi ola imodzi ndipo tikhala tikukambilana za moyo wanu wa tsiku ndi tsiku komanso zinthu zomwe zinakhuzha kupanga chiganizo/chisankho pankhani yakuziyeza wekha HIV.

Thank you for agreeing to spend time to answer some more detailed questions about yourself and your views of self-testing for HIV. This interview will probably take about one hour and we will be discussing the factors that influenced your decision to self-test as well as parts of your daily life.

A. HIV self-testing experience

1. Munasankha kuziyeza nokha, kusiyana ndikuyezedwa ndi anthu oyeza magazi. Mungandilongosolere chifukwa chomwe munasankhila njira yoziyeza wekha HIV?

You decided to self-test rather than take a provider-delivered HIV test. Could you talk to me about why you decided to self-test?

- ***Malingaliro okhuzha ndi kukhala pa chiopsyezo chotenga HIV? Kusintha kwa bwenzi? Chilimbikitso chochokera kwa bwenzi, kapena achibale? Kupezeka komanso mtengo wo gulira (transport, nthawi yobedwa/yotengedwa kuzochitika zine)?***

Perception of risk of HIV? Partner change? Support by partner or family? Accessibility and cost (e.g., convenience, transport and time taken from other activities)?

2. Mungandilongosolele mmene zinaliri kwa inuyo kuziyeza nokha?

Can you describe to me what was it like for you to self-test?

- ***Munkamva bwanji nthawi yomwe munkaziyeza?***
How did you feel during the self-testing process?
- ***Maganizo anu anali otani: pa chipangizo cho yezera? Kumveka kwa/kamvekedwe ka malangizo osatira? Kumveka kwa/kamvekedwe ka kuwerenga zotsatira zanu? Kalongezedwe ka chipangizo? Maonekedwe komanso kuphweka ka chipangizochoyezera?***

What did you think of the test kit in general? Clarity of instructions? Clarity of reading results? Packaging of the kit? Presentation and user friendliness of the kit?

3. Mungapereke malangizo otani kuti mchitidwe woziyeza uziyenda bwino?

What would you recommend to improve the experience?

4. Mungathe kuwalimbikisa anzanu ndi abale kuti aziyeze pogwilitsa ntchito njira yoziyeza wekha? Chifukwa chani?

Would you recommend self-testing to your friends or family? Why?

B. Previous experiences with HIV testing and health services

5. Munayamba mwayezetsapo HIV musanagwiritse ntchito njira yoziyeza wekha?

Have you ever had an HIV test before the self-test?

6. Mungandiwuze chifukwa chomwe munakayezetsera, ngati munayezetsa kopitilira kamodzi, munayezetsanso kenanso chifukwa chani?

If yes, can you explain why you decided to test or if you have tested more than once, what your reasons were for repeat testing?

- ***Malingaliro okhuzha ndi kukhala pa chiopsyezo chotenga HIV? Kusintha kwa bwenzi? Chilimbikitso chochokera kwa bwenzi, kapena achibale? Kupezeka komanso mtengo wo gulira (transport, nthawi yobedwa/yotengedwa kuzochitika zine)?***

- *Perception of risk of HIV? Partner change? Support by partner or family? Coerced testing? Accessibility and cost (e.g., convenience, transport and time taken from other activities)?*

7. Ngati munayayezetsapo, mwakhala mukukumana ndi zinthu zotani mukuyezetsa pogwiritsira ntchito njira zimenezi?



If yes, what has your experience been like with HIV testing services?

- ***Kapezekedwe komanso mtengo yake? Mtundu wa malo opereka chithandizo? Mtundu/ukachenjede wa anthu opereka chithandizo? Mtundu wa chithandizo (e.g. kupereka kwa munthu modzi, kapena kwa anthu amene ali paubwenzi pamodzi, njira yoyezetsera)? Ubwino wa chithandizo? Kukhulupilirana komanso kusunga chinsinsi (ubale pakati pa anthu opereka chithandizo komanso komanso olandira chithandizo komanso kulumikizana/kusiyana kwa mphamvu).***

Accessibility and cost? Type of facility? Type of staff? Type of services (e.g., individual or couples testing, type of test)? Quality of services? Trust and confidentiality (patient-provider relations & communication/power)?

8. Ngati simunayezetsepo, mungandilongoselere chifukwa chomwe munaganizira kuti musayezetse?

If no, can you explain why you decided not to test?

- ***Kapezekedwe komanso mtengo wake (e.g. kufupika kwa mtunda, transport, komanso kukana kuluza/kutaya zimena angapindule panthawi imene angawononge kupita kukayezesa)? Malingaliro awo pa chithandizo cha za umoyo? Malingaliro okhala pa chiopsyezo chotenga HIV? Kusowekera kwa chilimbikitso chochokera kwa bwenzi, kapena achibale? Mantha osalidwa ndi anthu? Mantha opezeka ndi kachilombo ka HIV?***

Accessibility and cost (e.g., convenience, transport and time taken from other activities)? Perception of health services? Perception of risk of HIV? Lack of support by partner or family? Fear of stigma or discrimination? Fear of being HIV positive?

C. Perceptions of risk

9. Muli ndi zodandaulitsa zilizonse zoti mutha kukhala pachiopsezo chotenga HIV, ngatinso zilipo zina zomwe zimakhuzza bwenzi lanu?

What concerns, if any, do you have about your risk of getting HIV? What about, if any, concerns for your partner?

10. Mungandilongosolere zinthu zokhuzana ndimoyo wanu zimene mumaona kuti zingachuluse chiopsyezo chanu chotenga HIV?

Can you describe to me what aspects in your life you consider likely to increase your risk of HIV?

11. Mungandilongosolere zinthu zokhuzana ndimoyo wanu, zimene mumaona kuti zingakuthandizeni kuti mu pewe HIV?

Can you describe to me what aspects in your life you consider likely to contribute to your avoidance of HIV?

12. Kodi mukuganiza kuti kukhala [munthu wa mamuna kapena mkazi] mudera lino kumatanthauza chani?

What do you think it means to be a [MAN or WOMAN] in this community?

- ***Kodi mukuganiza kuti maudindo ofunikira a [mamuna kapena mkazi] pakhomo ndi chani? Kodi ali ndi udindo wanji kumbali yosamalira thanzi lawo kapena la banja lawo?***

What do you think are the most important roles and responsibilities of a [MAN or WOMAN] in the household? What roles or responsibilities does [HE or SHE] often have when it comes to taking care of [HIS or HER] own health or the family's health?

13. Kodi kagawidwe ka zipangizo zoziyezela nokha kangakhale kotani kuti zipangozo zo zithe kufikira [AZIBAMBO / AZIMAYI] mdera lino? Nanga [AZIBAMBO / AZIMAYI] angathandizidwe motani kuti azitha kulandira thandizo panthawi imene apezeka ndi kachilombo ka HIV pamene aziyeza okha?

How can the distribution of self-test kits best reach [MEN or WOMEN] in this community? How can [MEN or WOMEN] best be supported to link to care if they get a positive self-result?

D. Distribution of HIV self-testing kits

14. Ndi zinthu ziti zomwe mungawonesese kuti zizichitika/mungakhazikise mutati inu mukufuna kukhazikitsa njira yatsopano yoyezera HIV mdera lanu?

If you could choose to design a new service for HIV testing, what are the components that you feel would be important to include that would persuade you to test?



- **Malo okayezetsera ndi mtengo woyezetsera? Mlingo wokuyang'anirani nthawi yoyezesa? Ntchito yama khasala/anthu opereka uphungu? Mtundu/njira yoziyezera? Uthenga womwe ziperekedwa? Nkhani yokhuzana ndi kusungirana chinsinsi?**
Location and cost? Level of supervision? Role of counsellors? Type of testing? Information provided? Issues surrounding confidentiality?

15. Pamene njira yoziyeza wekha yabwera m'dera lanu, mungakonde kupeza kachida koziyezera wekha kuchokera kwa ndani?

When self-testing becomes available in your community, how would you want to access the self-test kits?

- **Ndi ndani amene akuyenera kumagawa zipangizo zoziyezera wekha mu madera anu? (e.g. Ntchito/udindo, wamkazi/wamwamuna, zaka) Kutiko komanso nthawi yanji yimene anthu azipeza zipangizo zoziyezera wekha? (e.g. Kunyumba, M'dera, malo ogulitsira mankhwala; Matsiku ongwira ntchito, matsiku opuma) Pakuyenera kukhala kulumikizana ndi malo opereka chithandizo cha za umoyo ngati zipatala zazing'ono, malo oyesesa HIV a VCT, anthu oyendera ndi kugwira ntchito za chipatala mu Madera/a phungu/malo oyezetsera magazi ndi kulandila uphungu?**
Who should distribute self-test kits (e.g., occupation, sex, age)? Where and when should people be able to access self-test kits (e.g., home, community, pharmacy; weekdays, weekends)? What role/linkages should there be with health centres, VCT centres, HSAs, and counsellors?

16. Ndichithndizo chanji chomwe mungafune kulandila musanaziyeze nokha?

What type of information would you want to receive before self-testing?

17. Mungakonde mutalandira mlingo wanji woyang'anilidwa pamene mukuziyeza nokha pofuna kuonetsetsa kuti mwaziyeza mundodomeko yoyenelera?

What level of supervision would you want to make sure that the test is conducted properly?

18. Mungafune mutaloledwa kuti muwatengere abwenzi anu kachida kodziyezera okha HIV? Chifukwa chani mungafune kutero kapena kusatero?

Would you want to be allowed to take a self-testing kit for your partner? Why or why not?

- **Kodi ndi ubwino wanji kapena mavuto anji amene angabwere paubwenzi kamba kazimenezi?**
What potential problems or benefits could this introduce into the relationship?

E. Characteristics of HIV self-testing kit

19. Kudziyeza wekha kutha kuchitika pogwiritsa ntchito malovu kapena magazi. Ndimagazi, mutha kugwilitsa ntchito ka chida kodzibaya pa chala kuti mutenge magazi ndikuziyeza wekha HIV. Mungakonde kugwiritsa ntchito njira iti; yamkamwa kapena yodzitenga magazi?

Self-testing can be conducted using oral fluids or blood. With blood, you can use a finger prick test to collect your own small sample of blood and test yourself for HIV. What would you prefer for self-testing: an oral test or a blood-based test?

- **Kambilanani ubwino ndi kuyipa kwa njira iliyonse (mwachitsanzo. , ikani chidwi pa kuyenera kwake, kulondoloza kwake, kudzikhulupilira kuti mutha kudziyeza, kukhulupilira zotsatira ndi zina zotero.**
Discuss the advantages and disadvantages of each option (e.g., focus on convenience, accuracy, confidence in ability to conduct test, confidence in results, etc.)

20. Kodi mukuganiza kuti pali kusiyana kwanji komwe kuli kofunikira pakati pa kuziyeza wekha, ndikupita kokayezesa?

What do you think are the most important differences between self-testing and HTC?

21. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa kuyezetsa ku nyumba (wekha, kapena ndi aphungu oyezetsa) ndi kupita kukayezetsa ku malo oyezera?

What do you think are the most important differences between testing at home and testing at a facility?

F. HIV self-testing and counseling

22. Kodi mau oti 'uphungu' mumawamvetsa bwanji kumbali yoyezetsa HIV?



What do you understand by the term counselling in the context of HIV testing?

- **Kodi cholinga cha uphungu ndi chani? Akuyenera kupereka uphungu ndi ndani? Zikuyenera kukambidwa ndi chani? Anthu adzithandizidwa motani? Ndi mitundu iti ya uphungu (mwachitsanzo., wawekha, wa anthu awiri amene ali paubwenzi, wa banja) yomwe ikuyenera kupelekedwa?**
What is the purpose of counselling? Who should provide counselling? What should be discussed? How should people be supported? What types of counselling (e.g., individual, couple, family) should be provided?
- **Kodi uphungu ndi chimodzimodzi ndi kupereka uthenga kapena ndi zinthu zosiyana?**
Is counselling the same as information giving or different?

23. Kodi ndi mtundu uti wa uphungu omwe mungakonde mutalandira mutagwiritsa kale kapena musanagwiritse ntchito njira yoziyeza wekha?

What type of counselling, if any, would you want to receive before or after self-testing?

24. Kodi mukuonangati uphungu kapena uthenga okhuzana ndi njira yoziyeza wekha uziperekedwa ndi ndani? Uthengawu/umphungu, uziperekedwa bwanji (e.g ndi munthu, kapena pa phone)?

Who do you think should provide this information or counselling? How should this information or counselling be provided (e.g., in-person or telephone)?

G. HIV self-testing and linkage to care

25. Zomwe zingakuthandizeni kuti muzitha kutsimikiza, komanso kulumikizidwa ku chithandinzo, zosatira zanu zikaonetsa kuti muli ndikachilombo ka HIV.

What would help you to confirm your test if you received positive results after self-testing and link to support and care services?

H. HIV self-testing and safety concerns

26. Diziopsyezo zANJI zomwe mungamakumane nazo njira yakuziywza wekha itati ya khazikitsidwa mudera lanu?

What safety concerns would you have if self-testing was made available in your community?

- **Kuzipha? Kukakamizana kuti munthu ayezetse komanso aulule zosatira zake? Nkhanza kwa azimayi/azibambo?**
Coercive testing or disclosure? Gender-based violence?

I. Conclusion

27. Mutafuna kuzayezetsa mtsogolomu, mutha kuzasankha njira yiti yoyezesa? Chifukwa chani?

If you plan to test in the future, what kind of testing would you prefer? Why?

Zikomo kwambiri chifukwa cha nthawi yanu, kumbukirani kuti zonse zomwe takambiranazi ndi za chinsinsi. Ndaphunzirapo zambiri kuchokera mu zokambiranazi ndili ndi chikhulupiliro kuti nthawi imeneyi kwa inunso yakhala yofunikira.

Thank you very much for the time you have spent in answering my questions today. Please remember that this information is all confidential. I have learnt a lot from our discussion here today and hope that the time has also been useful to you.